GOVERNMENT OF MALAWI

MINISTRY OF AGRICULTURE, IRRIGATION AND WATER DEVELOPMENT

## SHIRE VALLEY TRANSFORMATION PROGRAMME-1
## CHIDZIWITSO CHAKUPELEKEDWA KWA CHIPUKUTA MSOZI

**MAWU OYAMBA**

**Boma la Malawi** kudzera mu **Unduna wa Zaulimi, Ulimi Wanthilira ndi Chitukuko cha Madzi** ndithandizo lochokera ku Bank ya Dziko Lonse (World Bank), African Development Bank ndi Global Environment Facility (GEF), likuyendetsa pulojekiti ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP). Pulojekiti ya SVTP idzabweretsa madzi anthilira mudera lokwanira ma hekitala 43, 370 kuchigwa cha Mtsinje wa Shire, m'maboma a Chikwawa ndi Nsanje.

Chingalande chotengela madzi chidzamangidwa kuchokera pa Damu la Kapichira m'Boma la Chikwawa mpaka ku Bangula, m'Boma la Nsanje. Izi zidzachititsa kuti madzi othilirira mbeu azipezeka chaka chonse mmadelawa. Ntchito yomanga ngalandezi zidzakhudza malo komanso katundu wa anthu. M'chaka cha 2018, Boma kudzela ku pulojekiti ya SVTP lidakhazikitsa ndondomeko imene imafotokozela mwatsatanetsatane njira zimene zayikidwa padela kuti miyoyo ya anthu amene akhudzidwe ndi pulojekitiyi isasokonezedwe. Ndondomekoyi makamaka ikufotokozela bwino njira zimene zizatsatidwe popeleka chipukuta msozi kwa anthu okhudzidwawa ndi kuonetsetsa kuti miyoyo yawo isasokonezedwe.

Boma la Malawi linakhazikitsa 15 Julaye, 2018 kukhala tsiku lomaliza kuti anthu achite kafukufuku okhudzana ndi nkhani za malo m'derali malingana ndi Malamulo a ndondomeko yotengela malo ochitira chitukuko ndi kaperekedwe ka chipukuta msozi (Land Acquisition and Compensation Act). Boma silidzapeleka chipukuta msozi pa chitukuko chilichonse chimene chinachitidwa tsikuli litadutsa.

Anthu oyenela kulandila chipukuta msozi anawelengedwa kudzela mu kawuniwuni amene adachitika nthawi imene ndondomekoyi inali kukonzedwa. Kawuniwuniyu adapeza kuti anthu 873 akuyenela kupeleka malo awo ku pulojekitiyi koma sadzasamutsidwa, mabanja 108 akuyenela kusamuka pamalo awo chifukwa chakuti chingalande chikudutsa m'mudzi mwawo, ndiponso mabanja ena 160 adzakhudzidwa chifukwa chakuti malo awo a bizinezi komanso malo ena amene amapezela zowathandizila pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku adzakhudzidwa. Anthu wovutika m'njira zosiyanasiyana okwanila 475 adzakhudzidwanso. Pali anthu okalamba 172, anthu aulumali 69, anthu odwalika 57, mabanja oyendetsedwa ndi amayi a masiye 114, mabanja oyendetsedwa ndi ana atatu (3) komanso anthu amene ali ndi kachilombo koyambitsa matenda a Edzi atatu (3). M'mwezi wa Januwale 2019, Unduna wa za Malo, Nyumba ndi Chitukuko cha M'matawuni unakatsimikizila katundu amene adzakhudzidwe ndi pulojekiti ya Shire Valley Transformation monga nyumba, mitengo, malo ndi zina zambiri.

**CHIDZIWITSO CHA CHIPUKUTA MSOZI**

Boma la Malawi kudzela mu Pulojekiti ya Shire Valley Transformation ndi Khonsolo ya Boma la Chikwawa motsogozedwa ndi Unduna wa za Malo, Nyumba ndi Chitukuko cha M'matawuni, likhala likudziwitsa onse okhudzidwa ndi pulojekitiyi tsatanetsatane wa chipukuta msozi chawo kuyambila pa 18 mpaka pa 29 November, 2019. Cholinga cha ntchitoyi chikhala kufotokozela zomwe zidapezeka pa kawuniwuni amene adachitika komanso ndalama zomwe zikuyenela kupelekedwa kwa munthu aliyense ngati chipukuta msozi. Anthu okhudzidwa adzasayinila makalata osonyeza kugwilizana ndi zomwe kawuniwuni adapeza komanso ndalama zomwe akuyenela kuti alandile ngati chipukuta msozi. Chipukuta msozi chisadapelekedwe zinthu izi zikuyenela kuchitika:

1. Kufotokozela anthu onse okhudzidwa za ndondomeko imene itsatidwe popeleka chipukuta msozi;
2. Kudziwitsa anthu okhudzidwa ndalama zimene akuyenela kulandila ngati chipukuta msozi;
3. Kuchititsa misonkhano kumidzi imene cholinga chake ndi kulangiza anthu okhudzidwa za kasamalidwe ndi kagwilitsidwe ntchito bwino ka ndalama;
4. Kuchita maphunzilo pa nkhani za kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo; ndi
5. Kutsekula mabuku aku banki.

Ndondomeko ya ntchitoyi idzapelekedwa kwa onse okhudzidwa komanso kwa adindo onse oyenelela.

Anthu onse okhudzidwa adapatsidwa mwayi wosankha pakati polandila chipukuta msozi ngati ndalama kapena kupatsidwanso katundu. Ndipo ubwino ndi kuyipa kwa njira ziwirizi kudawunikilidwa. Okhudzidwa amene adzasankhe chipukuta msozi cha ndalama akuyenera kudziwa zinthu izi:

1. Ndalama zonse zoposela K50,000 mpaka K100,000 zidzapatsidwa ngati cheke chimene ndalama zake akalandilile ku banki koma ngati ndalamazo ndi zochepela K50,000 ndalama zidzapelekedwa pamalo pomwepo.
2. Buku la ku banki lidzayenela kutsekulidwa kwa amene ndalama zawo ndi zoposela K100,000. A Khonsolo ya Boma la Chikwawa adzathandizila onse okhudzidwa kutsekula mabuku aku banki (akaunti) kuti ntchitoyi idzayende bwino. Anthu onse okhudzidwa akulimbikitsidwa kuti mabuku aku bankiwa adzatsekulidwe ngati banja (amai ndi abambo) pamene pali pofunika kutero. Amene alikale ndi ma akaunti adzagwilitsa ntchito ma akaunti omwewo.
3. Onse okhudzidwa akupemphedwa kubweretsa khadi la unzika kapena umboni wochokela kwa a mfumu pa nthawi imene chipukuta msozichi chidzakhale chikupelekedwa.

*Pulojekiti ya Shire Valley Transformation ikutsimikizila anthu onse okhudzidwa ndi dziko lonse la Malawi kuti:*

1. Anthu onse okhudzidwa adzalandila chipukuta msozi motengela ndi njira yomwe anasankha pakati pa ndalama kapena katundu wawo kubwezeletsedwa;
2. Ndalama zosamukila zapadera zidzapelekedwa kwa anthu okhudzidwa amene adzakhale ndi umboni weniweni kuti adasamukadi chifukwa cha pulojekiti;
3. Ndondomeko zayikidwa zowonetsetsa kuti miyoyo ya anthu onse okhudzidwa idzakhale ikuyenda monga mwa kale;
4. Ma komiti omva madandaulo a anthu okhudzana ndi pulojekiti ya Shire Valley Transformation adakhazikitsidwa ndipo akugwira ntchito. Cholinga cha makomitiwa ndikuwonetsetsa kuti madandaulo onse okhudzana ndi pulojekitiyi m'madera amene pulojekitiyi ikugwiramo ntchito adziweluzidwa kumudzi konko kuti pulojekiti isachedwetsedwe.

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri:*

1. Imbani foni pa nambala iyi : **01 828 709 (nthawi ya ntchito)**
2. Kapena kulemba kalata ya paintaneti kwa : **projectcoordinator@svtp.mw kapena info@svtp.mw**
3. Kapena lembani kalata kwa : **The Project Coordinator**
**Shire Valley Transformation Programme**
**P/Bag 379**
**Chichiri**
**Blantyre 3**

GOVERNMENT OF MALAWI

MINISTRY OF AGRICULTURE, IRRIGATION AND WATER DEVELOPMENT

## SHIRE VALLEY TRANSFORMATION PROGRAMME-1
## COMPENSATION DISCLOSURE NOTICE

**Background**

**The Government of Malawi (GoM)** through the **Ministry of Agriculture, Irrigation and Water Development,** with support from the World Bank, the African Development Bank and the Global Environment Facility (GEF), is implementing the Shire Valley Transformation Programme (SVTP). The Programme will develop 43,370 hectares of land for large scale irrigation agriculture in the Shire Valley, within the administrative districts of Chikwawa and Nsanje.

As part of the SVTP, irrigation canals will be constructed to enable the conveyance of irrigation water from Kapichira Dam on the Shire River to targeted farming areas within the two districts. Construction of the irrigation canals will affect people's land and property. In 2018, the SVTP prepared a Resettlement Action Plan (RAP) which details steps for ensuring minimization of impacts of physical and economic displacement of the Project Affected Persons (PAPs) in the Project locations. Specifically, the RAP outlines steps and arrangements for compensating Project Affected Persons (PAPs) and ensuring restoration and enhancement of their livelihoods.

The Government of Malawi further, set 15th July, 2018 as the cut-off date for all land and property surveys for land acquisition as per Section 6 of the Land Acquisition and Compensation Act (Cap. 58:04). All new property constructed within the demarcated and survey area and permanent developments or improvements done after the cut-off date will not be compensated.

The preparation of the RAP included a range of processes to determine the number of project affected persons to be compensated. It was established that the number of Project Affected Households that will lose land but will not be physically relocated is 873. Where the canal passes through villages, the number of households that will have their dwelling units physically relocated to other sites within the same villages is 108. The number of households that will be affected by non-land economic displacement (i.e. loss of structures, businesses, livelihoods, etc.) is 160.

The number of vulnerable PAPs is 475. These include the elderly (172), physically challenged (69); chronically ill (57), female heads (114), child heads (3) and HIV/AIDS (3). The Ministry of Lands, Housing and Urban Development conducted a verification exercise in January 2019 with all PAPs to confirm physical assets including land, trees, houses and properties to be compensated.

**Compensation Disclosure**

The Government of Malawi through the SVTP Programme Management Team, the Chikwawa District Council with support from the Ministry of Lands, Housing and Urban Development will conduct a compensation disclosure exercise to all PAPs from 18th to 29th November, 2019. The aim of the exercise will be to disclose and get agreement on assessed amount of compensation individual PAPs will receive.

*Prior to the actual payment of compensations following activities will have to be completed:*

1. Sensitization of the PAPs on the RAP process;
2. Disclosure of compensation to be received;
3. GVH and TA level meetings to counsel the PAPs;
4. Training on financial literacy and gender issues; and
5. Opening of Bank accounts.

The schedule for carrying out these activities will be distributed to all PAPs and all relevant stakeholders.

PAPs were already informed of the options of receiving compensations; either in-kind and in cash including the disadvantages and advantages of each option. PAPs also need to be aware that in case of opting for cash compensation:

1. Cash will be paid only where the compensation amount is **K50,000** or less.
2. For compensations of more than **K50,000** to **K100,000,** PAPs shall be paid using cheques cashable at local banks. For all compensations whose values exceed K100,000, the PAPs shall be required to open bank accounts and the District Commissioner's office would facilitate PAPs to open the accounts. PAPs are encouraged to open joint bank accounts with spouses where applicable. PAPs with existing bank accounts shall use the same accounts.
3. PAPs are also requested to bring national identity cards or evidence from the chief in case the card was lost for identification.

*All PAPs and the general public is assured that the Shire Valley Transformation Programme will ensure that:*

- Compensation should be paid to PAPs in accordance with their preference of option;
- The moving allowance will be dispensed to PAPs only where there is evidence of location and structures to be erected;
- There is a mechanism in place for follow up on the reconstruction of structures by PAPs;
- Grievance Redress committees that have been established are functional to ensure that grievances from PAPs and other people in the project area are addressed.

*For inquiries, please contact the following:*

1. Phone : **01 828 709**
2. E-mail : **projectcoordinator@svtp.mw copy info@svtp.mw**
3. Letter : **The Project Coordinator**
**Shire Valley Transformation Programme**
**P/Bag 379**
**Chichiri**
**Blantyre 3**